


# KUTHETSA NKHANZA KWA ANA

Kupewa, Kuteteza ndi Kuchitapo Kanthu

**(Kabuku ka Makolo komanso Adindo Osiyanasiyana M'madera)**

GOVERNMENT OF MALAWI
UNITED NATIONS MALAWI
Joint Programme on Girls Education

Norwegian Ministry of Foreign Affairs

Spotlight Initiative
To eliminate violence against women and girls

LAW COMMISSION
ENHANCING THE RULE OF LAW

## Mawu Oyamba

Kafukufuku wawonetsa kuti nkhanza zomwe ana amakumana nazo zikuchuluka m'dziko muno. Ana amakumana ndi nkhanza kunyumba, ku sukulu komanso munjira pamene akupita kapena kuchokera ku sukulu. Izi zili chomwechi chifukwa chakuti makolo komanso adindo ambiri samadziwa malamulo omwe amateteza ana ku nkhanza. Bukuli lakonzedwa ndi bungwe la Law Commission mogwirizana ndi Unicef pofuna kudziwitsa makolo komanso adindo za malamulo omwe amateteza ana ku nkhanza komanso kupereka njira zomwe makolo ndi adindo angagwiritse ntchito popewa ndi kuteteza mwana komanso kuchitapo kanthu pamene mwana wachitiridwa nkhanza. Ntchitoyi ikugwiridwa pansi pa ndondomeko ya *Safe Schools Programme* ndi thandizo lochokera ku Spotlight Initiative (SI) komanso United Nations Joint Programme on Girls Education (UNJPGE).

**Kodi Mwana ndi Ndani?**

Mwana ndi munthu amene sanakwanitse zaka 18. Malamulo amati makolo kapena munthu amene akulera mwana akuyenera kupereka chisamaliro ndi zinthu zofunikira kwa mwana posayang'anira kuti mwanayo anabadwa bwanji. Mwa zinthu zina, ana ali ndi ufulu wa: chitetezo; ulemu wachibadwidwe ndi kufunikira; moyo wabwino ndi kutukuka; kusamalidwa mofanana; kutenga nawo mbali kwathunthu pamagawo onse amoyo; komanso katundu (kuphatikizapo kulandira chuma chomwe chasiyidwa ndi makolo). Komabe, ana amakumana ndi mavuto ambiri kuphatikizapo nkhanza zomwe zimawalepheretsa kusangalala ndi maufulu awo. Buku lino likufotokoza nkhanza zomwe ana amakumana nazo ndi momwe anthu osiyanasiyana angathandizire kupewa, kuteteza komanso kuchitapo kanthu pa nkhanza zimenezo.

## MCHITIDWE WA NKHANZA KWA ANA

### *(a) Kulekelera ndi Kuthawa Ana*

Makolo ali ndi udindo wopereka chisamaliro ndi chitetezo kwa ana awo kuti akhale ndi moyo wabwino komanso akule. Kotero, makolo awonetsetse kuti ana akupita kusukulu, ali ndi chakudya, zovala, thandizo la mankhwala komanso pokhala, mwa zina. Kulephera kuwapatsa anawo zinthu zimenezi ndiye kulekelera; ndipo kuchoka ndikuwasiya ana opanda thandizo komanso owayang'anira ndiko kuthawa.

*Milandu ndi zilango zomwe zimaperekedwa molingana ndi kulekelera komanso kuthawa ana:*

| Mlandu | Chilango |
|---|---|
| Kulekelera | Kukhala kundende kwa zaka 7 |
| Kuthawa | Kukhala kundende kwa zaka 7 |
| Kulephera kupereka zinthu zofunikira | Kukhala kundende kwa zaka zitatu |

*Zoyenera kuchita pankhani yokhudza kulekelera ndi kuthawa:*

| Mdindo | Kupewa ndi Kuteteza | Kuchitapo Kanthu |
|---|---|---|
| Kholo | (a) Kutsogolera komanso kuzindikilitsa ana za kulekelera, kuthawa komanso kulephera kukwanilitsa udindo wa makolo;<br>(b) Kukhazikitsa chikhulupiriro ndi kudalirana pakati pa kholo ndi mwana kudzera kuonetsa chikondi ndi kupereka chisamaliro;<br>(c) Kuzindikira ufulu wa ana;<br>(d) Kulemekeza umunthu ndi kufunikira kwa ana;<br>(e) Kuchita kalondolondo wa kakulidwe ndi zochita za mwana;<br>(f) Kupereka zinthu zofunikira pa moyo kwa mwana;<br>(g) Kuonetsetsa kuti mwana akusamalidwa ndi munthu oyenera ngati kholo palibe; | (a) Kutsatira nkhani yomwe yachitika imene mwana wokhudzidwa kapena munthu wina wafotokoza;<br>(b) Ngati kulelekelera kapena kuthawa kwadza kamba ka kholo limodzi, kholo linalo liyenera kukasuma mchitidwe wakulelekera, kuthawa ndi kulephera kupereka zinthu |

| | | |
|---|---|---|
| | ndiponso<br>(h) Kulimbikitsa kusintha kwa zikhalidwe, miyambo, zikhulupiriro zoyipa ndi maganizidwe. | zofunikira, kwa adindo oyenera (amfumu, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, apolisi, ndi ena);<br>(c) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana wokhudzidwa; komanso<br>(d) Kutumiza ndi kuperekeza mwana wokhudzidwa kumalo amene akhoza kulandira thandizo (kwa mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, ku polisi, ku chipatala, kwa alangizi ndi ena). |
| Wachibale | (a) Kuzindikilitsa ana za kulekelera, kuthawa komanso kulephera kukwanilitsa udindo wa makolo;<br>(b) Kulimbikitsa kusintha kwa miyambo, ndi zikhalidwe zoyipa ndi zinthu zina;<br>(c) Kuzindikira ufulu wa ana;<br>(d) Kulemekeza umunthu ndi kufunikira kwa ana;<br>(e) Kuchita kalondolondo wa kakulidwe ndi zochita za mwana;<br>(f) Kupereka zinthu zofunikira pa moyo kwa mwana;<br>(g) Kuonetsetsa kuti mwana akusamalidwa ndi munthu woyenera ngati kholo palibe; ndiponso<br>(h) Kulimbikitsa kusintha kwa zikhalidwe, miyambo, zikhulupiriro zoyipa ndi maganizidwe. | (a) Kutsatira nkhani yomwe yachitika imene mwana wokhudzidwa kapena munthu wina wafotokoza;<br>(b) Ngati kulelekelera kapena kuthawa kwadza kamba ka kholo limodzi, kholo linalo liyenera kukasuma mchitidwe wakulelekera, kuthawa ndi kulephera kupereka zinthu zofunikira, kwa adindo oyenera (amfumu, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, apolisi, ndi ena);<br>(c) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana wokhudzidwa; komanso<br>(d) Kutumiza ndi kuperekeza mwana wokhudzidwa kumalo |

| | | |
|---|---|---|
| | | amene akhoza kulandira thandizo (kwa mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, alangizi, ku polisi, ku chipatala, ndi adindo ena) |
| Mfumu | (a) Kukhala patsogolo polimbikitsa ndi kutsogolera kusintha kwa chikhalidwe, miyambo ndi zina;<br>(b) Kukonza ndi kukwanilitsa ndondomeko zothandiza kuonetsetsa chitetezo, ubwino komanso kupita patsogolo kwa mwana;<br>(c) Kutsogolera ntchito yolimbikitsa ndi kuzindikilitsa anthu;<br>(d) Kukhazikitsa malamulo akudera olimbikitsa kuwonekera, kukhalapo komanso kuthandiza kwa makolo m'miyoyo ya ana awo; komanso pomwe pangafunikire, kulunzanitsa malamulo akudera omwe alipo ndi maufulu ndi zokomera ana; komanso;<br>(e) Kusuma zomwe zachitika kwa adindo oyenera (kupolisi, kwa mkulu waboma owona za chisamaliro cha anthu, utsogoleri wa pasukulu ndi ena). | Kutsogolera anthu ake ku ku adindo oyenera (kupolisi, utsogoleri wa pasukulu, mkulu wowona za chisamaliro cha anthu pa boma komanso ena) |
| Munthu wokhala m'dera | (a) Kuzindikira kuyipa kwa komanso milandu yokhudza kulekelera, kuthawa komanso kusachita zinthu zimene kholo limayenera kuchitira;<br>(b) Kugawana ndi anthu ena mauthenga okhudza kuyipa kwa kulekelera, kuthawa ndi kusachita zimene kholo limayenera kuchitira mwana;<br>(c) Kuvomereza ndi kulimbikitsa kusintha kwa zikhalidwe, miyambo, zikhulupiriro zoyipa ndi maganizidwe.;<br>(d) Kuvomereza, kuyikiza mwa ena ndi kulimbikitsa kukhala ndi udindo pa ana, aliyense payekhapayekha komanso pamodzi ngati gulu;<br>(e) Kupereke zinthu zofunikira pamoyo kwa mwana wosowa;<br>(f) Kuzindikira ndi kukhala tcheru ndi zinthu zina zomwe zingachitike zokhudza kulekelera, kuthawa komanso kusachita zimene kholo limayenera kuchitira mwana; komanso<br>(g) Kukonza ndi kukwanilitsa ndondomeko | (a) Kusuma mchitidwe wakulelekera, kuthawa ndi kulephera kupereka zinthu zofunkira, kwa adindo oyenera (amfumu, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, kupolisi, komanso kwa ena); komanso<br>(b) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana wokhudzidwa. |

| | | |
|---|---|---|
| | zolimbikitsira chitetezo, ubwino ndi kupita patsogolo kwa moyo wa mwana. | |
| Mphunzitsi ndi utsogoleri wa pa sukulu | (a) Kulimbikitsa anthu kuzindikira ndondomeko zoletsa mchitidwe wa kulekelera, kuthawa komanso kusachita zimene kholo limayenera kuchita;<br>(b) Kutsogolera ndi kuzindikilitsa ana za kulekelera, kuthawa komanso kulephera kukwanilitsa udindo kwa makolo;<br>(c) Kuzindikira ufulu wa ana;<br>(d) Kulemekeza umunthu ndi kufunikira kwa ana;<br>(e) Kuchita kalondolondo wa momwe mwana akukulira ndi zimene amakonda kuchita;<br>(f) Kulimbikitsa kusintha kwa zinthu;<br>(g) Kugwira ntchito mokwanira ndi anthu ena okhudzidwa (makolo, anthu akudera, amfumu, mkulu waboma owona za chisamaliro cha anthu, apolisi ndi ena);<br>(h) Kuvomereza, kukonza ndi kukwanilitsa ndondomeko zomwe cholinga chake ndi kuthana ndi mchitidwe wa kulekelera, kuthawa ndi kusachita zimene kholo liyenera kuchitira ana;<br>(i) Kukhazikitsa ndondomeko zoonetsetsa kuti ana akutetezedwa komanso akukhala bwino nthawi zonse; komanso<br>(j) Kuchita kalondolondo wankhani zomwe zasumidwa zokhudza kulekelera, kuthawa ndi kusachita zomwe kholo limayenera kuchitira ana. | (a) Kuthandiza mwana wokhudzidwa ndi kumutumiza kumalo amene akhoza kuthandizidwa (mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, mnzake, alangizi, ndi ena);<br>(b) Kuchita kalondolondo wa momwe mwana akuthandizidwira kumalo kumene mwanayo watumizidwa. |

***(b) Nkhanza za Chisembwere***

Nkhanza zachisembwere kwa mwana ndi mchitidwe wina uliwonse wokhudza kugonana ndi mwana. Zitsanzo za nkhanza za mtundu umenewu ndi izi: kugwilirira; kugonana ndi mwana wosakwana zaka 16; kuloleza kugonedwa kwa mwana pamalo; kuchita upo wogonana ndi mwana; kugonana ndi mwana yemwe ukumusamalira; ukumuyang'anira, womupeza ndi womusunga; kugonana pamalo pamene pali mwana; kuonetsa kapena kugulitsa mwana zinthu zolaula; kujambula mwana akuchita mchitidwe wogonana ndi kufalitsa zojambulazo; komanso kulankhula mawu kapena kumukhudza mwana malo obisika kusonyeza kumukhumba pa nkhani zokhudza kugonana.

Mchitidwe wina uliwonse umene umavomereza, kulimbikitsa kapena kuyika mwana pachiwopsezo chochitiridwa nkhanza za chisembwere uyenera kuthetsedwa.

*Milandu ndi zilango zomwe zimaperekedwa molingana ndi nkhanza za chisembwere:*

| Mlandu | Chilango |
|---|---|
| Kugwilirira | Kuphedwa kapena kukhala kundende moyo wake wonse |
| Kugonana ndi mwana | Kukhala kundende moyo wake wonse |
| Kuloleza kugonedwa kwa mwana pamalo | Kukhala kundende zaka zisanu |
| Kuchita upo wogonana ndi mwana | Kukhala kundende zaka zitatu |
| Kugonana ndi mwana yemwe ukumusamalira; ukumuyang'anira, womupeza ndi womusunga | Kukhala kundende zaka 21 |
| Kugonana pamalo pamene pali mwana | Kukhala kundende zaka 14 |
| Kuonetsa kapena kugulitsa mwana zinthu zolaula | Kukhala kundende zaka 7 |
| Kujambula mwana akuchita mchitidwe wogonana ndi kufalitsa zojambulazo | Kukhala kundende zaka 14 |
| Kulankhula mawu kapena kumukhudza mwana malo obisika kusonyeza kumukhumba mwana pa nkhani zokhudza kugonana | Kulipira chindapusa cha ndalama zokwana 1 miliyoni Kwacha ndi kukhala kundende zaka zisanu |

*Zoyenera kuchita pankhani zokhudza nkhanza za chisembwere:*

| Mdindo | Kupewa ndi Kuteteza | Kuchitapo Kanthu |
|---|---|---|
| Kholo | (a) Kutsogolera ndi kuzindikilitsa ana za nkhanza zachisembwere ndi momwe angazitetezere;<br>(b) Kukhazikitsa chikhulupiriro ndi kudalirana pakati pa kholo ndi mwana, kupyolera mu kuonetsa chikondi ndi chisamaliro;<br>(c) Kuzindikira ufulu wa ana;<br>(d) Kulemekeza umunthu ndi kufunikira kwa ana;<br>(e) Kuchita kalondolondo wa kakulidwe ndi zochita za mwana;<br>(f) Kupewa kutenga nawo mbali kapena kuwalola ana kutenga nawo mbali pa zikhalidwe zowopsa; kugonana ndi mwana wako wobereka wekha, mwana womupeza kapena wongomusunga; kuchita zachisembwere ndi mwana kapena pamalo pamene pali mwana; komanso kuwonetsa zinthu zokhudzana ndi kugonana ndi mwana; ndiponso kumujambula mwana akuchita mchitidwe wogonana ndi kufalitsa zojambulazo;<br>(g) Kuwauza ana kuti apewa kunyengereredwa;<br>(h) Kukhazikitsa kulumikizana kwapadera ndi kwa chinsinsi pakati pa kholo ndi mwana;<br>(i) Kuperekeza mwana kapena kutuma munthu wodalirika kuti aperekeze mwana popita ndi pochokera kusukulu kapena kumulimbikitsa mwana kuti adziyenda pagulu la anzake popita ndi pochokera kusukulu;<br>(j) Kuonetsetsa kuti mwana akusamalidwa ndi munthu woyenera pamene kholo palibepo; komanso<br>(k) Kulimbikitsa kusintha kwa zikhalidwe, miyambo, zikhulupiriro zoyipa ndi maganizidwe. | (a) Kutsatira nkhani yomwe yachitika imene mwana wokhudzidwa kapena munthu wina wafotokoza;<br>(b) Kusuma za mchitidwe wa nkhanza zachisembwere kwa adindo oyenera (amfumu, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, apolisi, bungwe loona za ufulu wa anthu, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena);<br>(c) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana wokhudzidwa; komanso<br>(d) Kutumiza ndi kuperekeza mwana wokhudzidwa kumalo amene akhoza kulandira thandizo (kwa mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma , apolisi, alangizi, ku chipatala, ndi adindo ena). |
| Wachibale | (a) Kutsogolera ndi kuzindikiritsa ana za nkhanza zachisembwere ndi momwe angadzitetezere;<br>(b) Kukhazikitsa chikhulupiriro ndi kudalirana pakati pa wachibale ndi mwana, kupyolera mu kuwonetsa chikondi ndi chisamaliro; | (a) Kutsatira nkhani yomwe yachitika imene mwana wokhudzidwa kapena munthu wina |

| | | |
|---|---|---|
| | (c) Kuzindikira ufulu wa ana;<br>(d) Kulemekeza umunthu ndi kufunikira kwa ana;<br>(e) Kuchita kalondolondo wa kakulidwe ndi zochita za mwana;<br>(f) Osatenga nawo mbali kapena kuwalola ana kutenga nawo mbali pa zikhalidwe zowopsya; kugonana ndi mwana wako wobereka wekha, mwana womupeza kapena wongomusunga; kuchita zachisembwere ndi mwana kapena pamalo pamene pali mwana; komanso kuonetsa zinthu zokhudzana ndi kugonana ndi mwana; ndiponso kumujambula mwana akuchita mchitidwe wogonana ndi kufalitsa zojambulazo;<br>(g) Kuwauza ana kuti azipewa kunyengereredwa;<br>(h) Kukhazikitsa kulumikizana kwapadera pakati pa wachibale ndi mwana;<br>(i) Kuperekeza mwana kapena kutuma munthu wina kuti aperekeze mwana popita ndi pochokera kusukulu kapena kumulimbikitsa mwana kuti adziyenda pagulu la anzake popita ndi pochokera kusukulu;<br>(j) Kuonetsetsa kuti mwana akusamalidwa ndi munthu wodalirika pamene kholo palibepo; komanso<br>(k) Kulimbikitsa kusintha kwa zikhalidwe, miyambo, zikhulupiriro zoyipa ndi maganizidwe. | wafotokoza;<br>(b) Kusuma za mchitidwe wa nkhanza zachisembwere kwa adindo oyenera (amfumu, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, apolisi, bungwe loona za ufulu wa anthu, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena);<br>(c) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana wokhudzidwa; komanso<br>(d) Kutumiza ndi kuperekeza mwana wokhudzidwa kumalo amene akhoza kulandira thandizo (kwa mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, apolisi, alangizi, ku chipatala, ndi adindo ena ). |
| Mfumu | (a) Kukhala patsogolo polimbikitsa ndi kutsogolera kusintha kwa zikhalidwe ndi miyambo yoyipa ndi zina;<br>(b) Kukonza ndi kukhazikitsa ndondomeko zothandiza kuonetsetsa chitetezo cha ana pamene akupita ndi kuchokera kusukulu, mwachitsanzo kutuma munthu wodalirika kuti aperekeze ana popita ndi pochokera kusukulu kapena kuwalimbikitsa ana kuti aziyenda m'magulu popita ndi pochokera kusukulu;<br>(c) Kutsogolera ntchito yolimbikitsa ndi kuzindikiritsa anthu;<br>(d) Kukonza kapena kulunzanitsa malamulo akudera ndi malamulo oletsa nkhanza | Kuwatsogolera anthu ake kumalo komwe angakathandizidwe (kwa mkulu waboma woona zachisamaliro cha anthu, kupolisi, ofesi yoona za ufulu wa anthu, mkulu womva za madandaulo a anthu ndi ena. |

| | | |
|---|---|---|
| | zachisembwere; komanso<br>(e) Kusuma mchitidwe wa nkhanza kwa mwana kwa adindo oyenera (utsogoleri wa pasukulu, mkulu waboma woona za chisamaliro cha anthu, ofesi yoona za ufulu wa anthu, mkulu wa ofesi yomva za madandaulo a anthu ndi ena. | |
| Munthu wokhala m'dera | (a) Kutsata malamulo okhudza nkhanza zachisembwere;<br>(b) Kugawana ndi anthu ena mauthenga okhudza kuopsya kwa nkhanza zachisembwere;<br>(c) Kuvomereza ndi kulimbikitsa kusintha kwa maganizidwe;<br>(d) Kuvomereza ndi kulimbikitsa udindo wosamala ana, ngati gulu mothandizana kapena aliyense payekhapayekha;<br>(e) Kupewa kutenga nawo mbali kapena kuchititsa kuti ana atenge mbali pa zikhalidwe zoopsya; kugonana; kapena kuchita zachisembwere pamalo pomwe pali mwana; komanso kuonetsa kapena kugulitsa zinthu zokhudzana ndi kugonana ndi mwana; ndi kumujambula mwana akuchita mchitidwe wogonana ndi kufalitsa zojambulazo;<br>(f) Kuzindikira ndi kukhala tcheru ndi zochitika zina zokhudza nkhanza zachisembwere; komanso<br>(g) Kukonza ndi kukwanilitsa ndondomeko zoonetsetsa kuti mwana ndiwotetezedwa kunyumba, kusukulu komanso pamene akuyenda kupita ndi kuchokera kusukulu. | (a) Kusuma mchitidwe wa nkhanza zachisembwere kwa adindo oyenera (kwa a mfumu, apolisi, mkulu wowona za chisamaliro cha anthu pa boma , mabungwe omwe siaboma, bungwe loona za ufulu wa anthu, mkulu womva madandaulo a anthu ndi ena; komanso<br>(b) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana wokhudzidwa. |
| Mphunzitsi ndi utsogoleri wa pasukulu | (a) Kukonza ndi kukhazikitsa ndondomeko zothandiza kuonetsetsa chitetezo cha ana pamene akupita ndi kuchokera kusukulu, mwachitsanzo kutuma munthu wodalirika kuti aperekeze ana popita ndi pochokera kusukulu kapena kuwalimbikitsa ana kuti aziyenda m'magulu popita ndi pochokera kusukulu;<br>(b) Kulimbikitsa malamulo othana ndi mchitidwe wa nkhanza zachisembwere;<br>(c) Kuwatsogolera ndi kuzindikiritsa ana za nkhanza zachisembwere ndi momwe angazitetezere;<br>(d) Kulimbikitsa makolo kuti akhazikitse kulumikizana kwapadera kwachinsinsi ndi ana awo;<br>(e) Kuzindikira ufulu wa ana;<br>(f) Kulemekeza umunthu ndi kufunikira kwa ana;<br>(g) Kuchita kalondolondo wa mmene akukulira mwana ndi zochita za mwana;<br>(h) Kulimbikitsa ndi kutsogolera ntchito yothetsa nkhanza za chisembwere kwa ana; | (a) Kusuma mchitidwe wa nkhanza zachisembwere kwa adindo oyenera (kwa a mfumu, apolisi, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, mabungwe omwe siaboma, bungwe loona za ufulu wa anthu, mkulu womva madandaulo a anthu ndi ena;<br>(b) Kulimbikitsa chilango kwa mphunzitsi kapena mkulu woyendetsa ntchito zapasukulu; komanso<br>(c) Kuthandiza ndi |

| | | |
|---|---|---|
| | (i) Kugwira ntchito mokwanira ndi mafumu, apolisi, makolo ndi anthu akudera;<br>(j) Kuvomereza, kukonza ndi kukwanilitsa ndondomeko zomwe cholinga chake ndi kuthana ndi mchitidwe wa nkhanza za chisembwere;<br>(k) Kupewa kutenga mbali kapena kuchititsa kuti ana atenge mbali pa zikhalidwe zoopsya; kugonana; kapena kuchita zachisembwere pamalo pomwe pali mwana; komanso kuonetsa kapena kugulitsa zinthu zokhudzana ndi kugonana ndi mwana; ndi kumujambula mwana akuchita mchitidwe wogonana ndi kufalitsa zojambulazo;<br>(l) Kukhazikitsa ndondomeko zothandiza okhudzidwa kunena komanso kugawana ntchito;<br>(m) Kukhazikitsa ndondomeko zoonetsetsa kuti ana akutetezedwa nthawi zonse; komanso<br>(n) Kuchita kalondolondo wankhani zomwe zasumidwa zokhudza nkhanza zachisembwere. | kutumiza mwana wokhudzidwa kwa adindo ndi mabungwe oyenera omwe angamuthandize (mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, mphunzitsi, mnzake, wogwira ntchito za umoyo, mlangizi, ndi ena). |

### *(c) Nkhanza Zosakhudza Chisembwere*

Nkhanza zosakhudza chisembwere ndiko kuchita kapena kulephera kuchita chinthu, zomwe mapeto ake zimayika pachiopsyezo umoyo wa mwana kuthupi, kakhalidwe ndi anthu ena, kaganizidwe, kapezedwe ka chuma, umoyo, ndi kakulidwe ka mwanayo. Izi ndi monga: kuwumiliza kuchita zinthu; kuonetsa kapena kugulitsa zinthu zoyipa (monga zinthu zokhudza kugonana, mankhwala ozunguza bongo, nkhanza, kapena zina zilizonse zosokoneza maganizo).

Kuonetsa kapena kugulitsa zinthu zoyipa ndi mlandu umene chilango chake ndi kukhala kundende kwa zaka 7.

*Zoyenera kuchita pankhani zokhudza nkhanza zosakhudza chisembwere:*

| Mdindo | Kupewa ndi kuteteza | Kuchitapo Kanthu |
|---|---|---|
| Kholo | (a) Kutsogolera ndi kuzindikilitsa ana za nkhanza zosakhudza chisembwere ndi momwe angadzitetezere;<br>(b) Kukhazikitsa chikhulupiriro ndi kudalirana pakati pa kholo ndi mwana, kudzera mu kuonetsa chikondi ndi chisamaliro;<br>(c) Kuzindikira ufulu wa ana;<br>(d) Kulemekeza umunthu ndi kufunikira kwa ana;<br>(e) Kuchita kalondolondo wa kakulidwe ndi zochita za mwana;<br>(f) Kupewa kuonetsa kapena kugulitsa mwana zinthu zoyipa (mankhwala osokoneza | (a) Kutsatira nkhani yomwe yachitika imene mwana wokhudzidwa kapena munthu wina wafotokoza;<br>(b) Kusuma za mchitidwe wa nkhanza kwa adindo oyenera (amfumu, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, apolisi, bungwe |

| | | |
|---|---|---|
| | bongo, zinthu zokhudza umbanda, chisembwere, nkhanza, kapena zina zilizonse zoyipa)<br>(g) Kuonetsetsa kuti mwana akusamalidwa ndi munthu woyenera pamene kholo palibepo;<br>(h) Kulimbikitsa kusintha kwa zikhalidwe, miyambo, zikhulupiriro zoyipa ndi maganizidwe; komanso<br>(i) Kuperekeza mwana kapena kutuma munthu wina kuti aperekeze mwana popita ndi pochokera kusukulu kapena kumulimbikitsa mwana kuti adziyenda pagulu la anzake popita ndi pochokera kusukulu. | loona za ufulu wa anthu, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena);<br>(c) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana wokhudzidwa; komanso<br>(d) Kutumiza ndi kuperekeza mwana wokhudzidwa kumalo amene akhoza kulandira thandizo (kwa mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, alangizi, ku polisi, ku chipatala, ndi adindo ena). |
| Wachibale | (a) Kutsogolera ndi kuzindikilitsa ana za nkhanza zosakhudza chisembwere ndi momwe angadzitetezere;<br>(b) Kuzindikira ufulu wa ana;<br>(c) Kukhazikitsa chikhulupiriro ndi kudalirana pakati pa kholo ndi mwana, kudzera mu kuonetsa chikondi ndi chisamaliro;<br>(d) Kulemekeza umunthu ndi kufunikira kwa ana;<br>(e) Kuchita kalondolondo wa kakulidwe ndi zochita za mwana;<br>(f) Kupewa kuwonetsa kapena kugulitsa mwana zinthu zoyipa (mankhwala osokoneza bongo, zinthu zokhudza umbanda, chisembwere, nkhanza, kapena zina zilizonse zoyipa);<br>(g) Kukhazikitsa malo ndi ndondomeko zogawira mauthenga okhudza nkhanza zosakhudza chisembwere pakati pa anthu am'banja;<br>(h) Kuonetsetsa kuti mwana akusamalidwa ndi munthu woyenera pamene kholo palibepo;<br>(i) Kupereka zinthu zofunikira zokwanira kwa mwana;<br>(j) Kuperekeza mwana kapena kutuma munthu wodalirika kuti aperekeze mwana popita ndi pochokera kusukulu kapena kumulimbikitsa mwana kuti adziyenda pagulu la anzake popita ndi pochokera kusukulu; komanso | (e) Kutsatira nkhani yomwe yachitika imene mwana wokhudzidwa kapena munthu wina wafotokoza;<br>(f) Kusuma za mchitidwe wa nkhanza kwa adindo oyenera (amfumu, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, apolisi, bungwe loona za ufulu wa anthu, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena);<br>(g) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana wokhudzidwa; komanso<br>(h) Kutumiza ndi kuperekeza mwana wokhudzidwa kumalo amene akhoza kulandira thandizo (kwa mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, alangizi, ku polisi, ku chipatala, ndi |

| | | |
|---|---|---|
| | (k) Kulimbikitsa kusintha kwa zikhalidwe, miyambo, zikhulupiriro zoyipa ndi maganizidwe. | adindo ena). |
| Munthu wokhala m'dera | (a) Kutsata malamulo okhudza nkhanza zosakhudza chisembwere;<br><br>(b) Kugawana ndi anthu ena mauthenga okhudza kuopsya kwa nkhanza zosakhudza chisembwere;<br><br>(c) Kuvomereza ndi kulimbikitsa kusintha kwa maganizidwe;<br><br>(d) Kuvomereza, kuyikiza mwa ena ndi kulimbikitsa udindo wosamala ana, ngati gulu mothandizana kapena aliyense payekhapayekha;<br><br>(e) Kukhazikitsa malo ndi ndondomeko zogawirana mauthenga a nkhanza zosakhudza chisembwere pakati pa anthu akudera;<br><br>(f) Kupewa kuonetsa kapena kugulitsa mwana zinthu zoyipa (mankhwala osokoneza bongo, zinthu zokhudza umbanda, chisembwere, nkhanza, kapena zina zilizonse zoyipa);<br><br>(g) Kuzindikira ndi kukhala tcheru ndi zinthu zina zomwe zingachitike zokhudza mchitidwe wa nkhanza zosakhudza chisembwere; komanso<br><br>(h) Kukonza ndi kukwanilitsa ndondomeko zoonetsetsa kuti mwana ndiwotetezedwa kunyumba, kusukulu komanso pamene akuyenda kupita ndi kuchokera kusukulu, mwachitsanzo, kutuma munthu wodalirika kuti aperekeze ana popita ndi kuchokera kusukulu kapena kuwalimbikitsa ana kuti adziyenda m'magulu popita ndi pochokera kusukulu. | (i) Kusuma mchitidwe wa nkhanza zachisembwere kwa adindo oyenera (kwa a mfumu, apolisi, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, mabungwe omwe si aboma, bungwe loona za ufulu wa anthu, mkulu womva madandaulo a anthu ndi ena; komanso<br>(j) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana wokhudzidwa. |
| Mphunzitsi ndi utsogoleri wa pasukulu | (a) Kukonza ndi kukhazikitsa ndondomeko zothandiza kuonetsetsa chitetezo cha ana pamene akupita ndi kuchokera kusukulu. Mwachitsanzo, kutuma munthu kuti aperekeze ana popita ndi pochokera kusukulu kapena kuwalimbikitsa ana kuti | (k) Kusuma mchitidwe wa nkhanza zachisembwere kwa adindo oyenera (kwa a mfumu, kupolisi, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, |

| | | |
|---|---|---|
| | aziyenda m'magulu popita ndi pochokera ku sukulu;<br>(b) Kulimbikitsa malamulo othana ndi mchitidwe wa nkhanza zosakhudza chisembwere ndi momwe angadzitetezere;<br>(c) Kulimbikitsa makolo kuti akhazikitse kulumikizana kwapadera kwachinsinsi ndi ana awo;<br>(d) Kuzindikira ufulu wa ana;<br>(e) Kulemekeza umunthu ndi kufunikira kwa ana;<br>(f) Kuchita kalondolondo wa kakulidwe ndi zochita za mwana;<br>(g) Kulimbikitsa ndi kutsogolera ntchito yothetsa nkhanza zosakhudza chisembwere kwa ana;<br>(h) Kugwira ntchito ndi mafumu, apolisi, makolo ndi anthu akudera;<br>(i) Kuvomereza, kukonza ndi kukwanilitsa ndondomeko zomwe cholinga chake ndi kuthana ndi mchitidwe wa nkhanza zosakhudza chisembwere;<br>(j) Kukhazikitsa ndondomeko zodziwitsirana ndi kugawana ntchito;<br>(k) Kukhazikitsa ndondomeko zowonetsetsa kuti ana akutetezedwa nthawi zonse; komanso<br>(l) Kuchita kalondolondo wankhani zomwe zasumidwa zokhudza nkhanza zosakhudza chisembwere. | mabungwe omwe si aboma, bungwe loona za ufulu wa anthu, mkulu womva madandaulo a anthu ndi ena;<br>(l) Kulimbikitsa chilango kwa mphunzitsi kapena mkulu woyendetsa ntchito za pa sukulu; komanso<br>(m) Kuthandiza ndi kutumiza mwana wokhudzidwa kwa adindo ndi mabungwe oyenera omwe angamuthandize ( mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, mphunzitsi, mnzake, wogwira ntchito zaumoyo, mlangizi, ndi ena). |

### *(d) Kugwiritsa Ntchito Ana Mosayenera*

Kugwiritsa ntchito ana mosayenera ndiko kugwiritsa ntchito mwana ngati chinthu chopezera phindu; kugwiritsa ntchito mwana (momuwumiriza kapena mwakufuna kwake); kugonana ndi mwana; Kukakamiza mwana kugwira ntchito yomwe phindu lake limapita kwa makolo, munthu omusunga kapena wina aliyense; ukwati wa mwana (womukakamiza kapena kufuna iye asanafike msinkhu woyenera kukwatira kapena

kukwatiwa); komanso kugwiritsa ntchito mwana kusangalatsa anthu munjira zosavomelezeka pachikhalidwe, zoopsyeza moyo, thanzi, mphamvu ndi zina zotero.

*Milandu ndi zilango zomwe zimaperekedwa mokhudzana ndi kugwiritsa ntchito ana mosayenera:*

| Mlandu | Chilango |
| --- | --- |
| Kugwiritsa ntchito mwana | Kulipira chindapusa cha ndalama zokwana K20, 000 ndi kukhala kundende kwa zaka zisanu |
| Kukwatira kapena kuumiriza mwana kulowa m'banja | Kukhala kundende kwa zaka 10 |
| Kukakamiza mwana kugwira ntchito yomwe phindu lake limapita kwa makolo, munthu omusunga kapena wina aliyense | Kukhala kundende kwa zaka 10 |
| Kugwiritsa ntchito mwana kuti atenge mbali muzinthu zosangalatsa anthu munjira zosavomelezeka pachikhalidwe komanso zoopsyeza moyo, thanzi, mphamvu ndi zina zotero. | Kulipira chindapusa cha ndalama zokwana K100,000 ndi kukhala kundende kwa zaka 7 |
| | Kutsekedwa kwa malo a chisangalalo kwa kanthawi kapena kulandidwa chiphaso chochitira malonda |

*Zoyenera kuchita pankhani yokhudza kugwiritsa ntchito ana mosayenera:*

| Mdindo | Kupewa ndi Kuteteza | Kuchitapo Kanthu |
| --- | --- | --- |
| Kholo | (a) Kulangiza ana ndi kuwazindikilitsa za kugwiritsa ntchito ana mosayenera ndi momwe angadzitetezere;<br>(b) Kukhazikitsa kulumikizana kwapadera kwachinsinsi pakati pa kholo ndi mwana;<br>(c) Kukhazikitsa chikhulupiriro ndi kudalirana pakati pa kholo ndi mwana, kudzera mu kuonetsa chikondi ndi chisamaliro;<br>(d) Kuzindikira ufulu wa ana;<br>(e) Kulemekeza umunthu ndi kufunikira kwa ana;<br>(f) Kuchita kalondolondo wa kakulidwe ndi zochita za mwana;<br>(g) Kupereka zinthu zoyenerera zokwanira kwa mwana, kuphatikizapo zomwe zaperekedwa kudzera mu wilo;<br>(h) Kupewa kutenga nawo mbali muzikhalidwe zoyipa; kugwiritsa ntchito | (a) Kutsatira nkhani yomwe yachitika imene mwana wokhudzidwa kapena munthu wina wafotokoza;<br>(b) Kusuma za mchitidwe wa nkhanza zogwiritsa nchito mwana mosayenera kwa adindo oyenera (amfumu, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, kupolisi, bungwe loona za ufulu wa anthu, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena); komanso |

| | | |
|---|---|---|
| | mwana kuti atenge nawo mbali muzinthu zosangalatsa anthu munjira zosavomelezeka pachikhalidwe, zoopsyeza moyo, thanzi ndi mphamvu; ndi zina zotere;<br>(i) Kuonetsetsa kuti mwana akusamalidwa ndi munthu woyenera pamene kholo palibepo;<br>(j) Kupereka zinthu zoyenera zokwanira kwa mwana;<br>(k) Kuperekeza mwana kapena kutuma munthu wodalirika kuti aperekeze mwana popita ndi pochokera kusukulu kapena kumulimbikitsa mwana kuti adziyenda pagulu la anzake popita ndi pochokera kusukulu; komanso<br>(l) Kulimbikitsa kusintha kwa zikhalidwe, miyambo, zikhulupiriro zoyipa ndi maganizidwe. | (c) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana wokhudzidwa. |
| Wachibale | (a) Kukhazikitsa kulumikizana kwapadera kwachinsinsi pakati pa wachibale ndi mwana;<br>(b) Kuwatsogolera ndi kuzindikiritsa ana za kugwiritsa ntchito ana mosayenera ndi momwe angadzitetezere;<br>(c) Kuzindikira ufulu wa ana;<br>(d) Kulemekeza umunthu ndi kufunikira kwa ana;<br>(e) Kuchita kalondolondo wa kakulidwe ndi zochita za mwana;<br>(f) Kupewa kutenga nawo mbali mu zikhalidwe zoyipa; kugwiritsa ntchito mwana kuti atenge nawo mbali muzinthu zosangalatsa anthu munjira zosavomelezeka pachikhalidwe, zoopsyeza moyo, thanzi ndi mphamvu; ndi zina zotere;<br>(g) Kupereka zinthu zoyenera zokwanira kwa mwana;<br>(h) Kuperekeza mwana kapena kutuma munthu wodalirika kuti aperekeze mwana popita ndi pochokera kusukulu kapena kumulimbikitsa mwana kuti adziyenda pagulu la anzake popita ndi pochokera kusukulu; komanso<br>(i) Kulimbikitsa kusintha kwa zikhalidwe, miyambo, zikhulupiriro zoyipa ndi maganizidwe. | (a) Kutsatira nkhani yomwe yachitika imene mwana wokhudzidwa kapena munthu wina wafotokoza;<br>(b) Kusuma za mchitidwe wa nkhanza zogwiritsa nchito mwana mosayenera kwa adindo oyenera (amfumu, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, apolisi, bungwe loona za ufulu wa anthu, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena); komanso<br>(c) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana wokhudzidwa. |

| | | |
|---|---|---|
| Amfumu | (a) Kukhala patsogolo polimbikitsa ndi kutsogolera kusintha kwa chikhalidwe, miyambo ndi zina;<br>(b) Kutsogolera ntchito yolimbikitsa ndi kuzindikiritsa anthu;<br>(c) Kukonza kapena kuluzanitsa malamulo akudera ndi malamulo oletsa mchitidwe wogwiritsa ntchito ana mosayenera;<br>(d) Kulimbikitsa malamulo olimbana ndi mchitidwe wogwiritsa ntchito ana mosayenera;<br>(e) Kukonza ndi kukhazikitsa ndondomeko zothandiza kuonetsetsa chitetezo cha ana pamene akupita ndi kuchokera kusukulu, mwachitsanzo kutuma munthu kuti aperekeze ana popita ndi pochokera kusukulu kapena kuwalimbikitsa ana kuti aziyenda m'magulu popita ndi pochokera kusukulu; komanso<br>(f) Kusuma zomwe zachitika kwa anthu oyenera (utsogoleri wa pasukulu, mkulu waboma woona za chisamaliro cha anthu, ofesi yowona za ufulu wa anthu, mkulu wa ofesi yomva za madandaulo a anthu ndi ena). | (a) Kulimbikitsa malamulo olangila anthu olakwa ngati alipo;<br>(b) Kutsogolera anthu ake kumaofesi oyenera (kupolisi, utsogoleri wa pasukulu, mkulu waboma woona za chisamaliro cha anthu ndi ena); komanso<br>(c) Kusuma mchitidwe wogwiritsa ntchito ana mosayenera kwa adindo oyenera (unduna wa zamaphunziro, bungwe loona za ufulu wa anthu, ofesi ya mkulu womva za madandaulo a anthu ndi kwina); |
| Munthu wokhala m'dera | (a) Kutsata malamulo okhudza kugwiritsa ntchito ana mosayenera<br>(b) Kugawana ndi anthu ena mauthenga okhudza kuopsya kwa kugwiritsa ntchito ana mosayenera;<br>(c) Kuvomereza ndi kulimbikitsa kusintha kwa maganizidwe;<br>(d) Kuvomereza, kuyikiza mwa ena ndi kulimbikitsa udindo wosamala ana, ngati gulu mothandizana kapena aliyense payekhapayekha;<br>(e) Kupewa kutenga nawo mbali mu zikhalidwe zoyipa; kugwiritsa ntchito mwana kuti atenge nawo mbali muzinthu zosangalatsa anthu munjira zosavomelezeka pachikhalidwe, zoopsyeza moyo, thanzi ndi mphamvu; ndi zina zotere;<br>(f) Kuzindikira ndi kukhala tcheru ndi zinthu zina zomwe zingachitike zokhudza mchitidwe wogwiritsa ntchito ana molakwika; komanso<br>(g) Kukonza ndi kukwanilitsa ndondomeko zoonetsetsa kuti mwana ndiwotetezedwa kunyumba, kusukulu komanso pamene | (a) Kusuma mchitidwe wogwiritsa ntchito ana mosayenera kwa adindo oyenera (kwa a mfumu, apolisi, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, mabungwe omwe siaboma, bungwe loona za ufulu wa anthu, mkulu womva madandaulo a anthu ndi ena); komanso<br>(b) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana wokhudzidwa. |

| | | |
|---|---|---|
| | akuyenda kupita ndi kuchokera kusukulu, mwachitsanzo kutuma munthu wodalirika kuti aperekeze ana popita ndi kuchokera kusukulu kapena kuwalimbikitsa ana kuti adziyenda m'magulu popita ndi pochokera kusukulu. | |
| Mphunzitsi ndi utsogoleri wa pasukulu | (a) Kutsogolera ndi kuzindikilitsa ana za kugwiritsa ntchito ana mosayenera ndi momwe angadzitetezere<br>(b) Kuzindikira ufulu wa ana;<br>(c) Kulemekeza umunthu ndi kufunikira kwa ana;<br>(d) Kuchita kalondolondo wa kakulidwe ndi zochita za mwana;<br>(e) Kulimbikitsa ndi kutsogolera ntchito yolimbana ndi mchitidwe wogwiritsa ntchito ana mosayenera;<br>(f) Kugwira ntchito ndi mafumu, apolisi, makolo ndi anthu akudera);<br>(g) Kuvomereza, kukonza ndi kukwanilitsa ndondomeko zomwe cholinga chake ndi kuthana ndi mchitidwe wogwiritsa ntchito ana mosayenera;<br>(h) Kusuma mchitidwe wogwiritsa ntchito ana mosayenera kwa anthu ndi mabungwe oyenera (apolisi, ofesi ya mkulu waboma woona za chisamaliro cha anthu, ofesi yowona za ufulu wa anthu, ofesi yomva madandaulo a anthu ndi ena);<br>(i) Kukhazikitsa ndondomeko zothandiza ana okhudzidwa kukanena komanso kugawana ntchito;<br>(j) Kukonza ndi kukhazikitsa ndondomeko zothandiza kuonetsetsa chitetezo cha ana pamene akupita ndi kuchokera kusukulu, mwachitsanzo kutuma munthu kuti aperekeze ana popita ndi pochokera kusukulu kapena kuwalimbikitsa ana kuti aziyenda m'magulu popita ndi pochokera kusukulu; komanso<br>(k) Kuchita kalondolondo wankhani zomwe zasumidwa zokhudza kugwiritsa ntchito ana mosayenera. | (a) Kulimbikitsa malamulo olangila anthu olakwa ngati alipo;<br>(b) Kuthandiza ndi kutumiza mwana wokhudzidwa kwa adindo ndi mabungwe oyenera omwe angamuthandize (mkulu owona za chisamaliro cha anthu pa boma, mphunzitsi, mnzake, wogwira ntchito za umoyo, mlangizi, ndi ena); komanso<br>(c) Kusuma mchitidwe wogwiritsa ntchito ana mosayenera kwa adindo oyenera (ku unduna wa zamaphunziro, ku polisi, kwa mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, ku bungwe loona za ufulu wa anthu, ku ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu ndi ena). |
| Abambo olimbikitsa ntchito zolimbana ndi mchitidwe | (a) Kulimbikitsa ndi kuzindikiritsa anthu;<br>(b) Kutsogolera kusintha kwa maganizidwe a anthu<br>(c) Kukhazikitsa ndondomeko zothandiza anthu kuphunzira ndi kukambilana; komanso | (a) Kusuma ndi kutumiza wokhudzidwa ndi mchitidwe wogwiritsa ntchito ana mosayenera kwa adindo ndi maofesi oyenera; |

| | | |
|---|---|---|
| oyipa mmudzi (Male Champion) | (d) Kuthandiza ndi kulangiza makolo, anthu osunga ana, atsogoleri a pasukulu ndi mafumu pamene akuthana ndi nkhani zokhudza kugwiritsa ntchito ana mosayenera. | (b) Kutsatira nkhani yomwe yachitika ndipo yatumizidwa ku maofesi oyenera; komanso<br>(c) Kudzudzula mchitidwe wogwiritsa ntchito ana mosayenera, ngati nkoyenera kutero. |

### *(e) Kulanda Chuma Chamasiye*

Kulanda chuma cha masiye ndiwo mchitidwe wolanda katundu wamasiye, motsutsana ndi malamulo, kuchokera kwa munthu yemwe ayenera kupindula ndi katunduyo, kuphatikizapo mwana. Mwana wina aliyense wa malemu kuphatikizapo ana obadwira ku banja la mseli kaya kuchibwenzi akuyenera kulandira chuma chamasiye. Kulanda katundu wamasiye ndi mlandu waukulu womwe chilango chake ndi kukakhala kundende zaka 10 ndikulipira chindapusa cha ndalama zosachepera mtengo wa katundu yemwe analandidwayo.

*Zoyenera kuchita pankhani zokhudza kulanda katundu:*

| Mdindo | Kupewa ndi Kuteteza | Kuchitapo Kanthu |
|---|---|---|
| Kholo | (a) Konzani wilo; komanso<br>(b) Tambasulani momveka bwino magawidwe a katundu. | Kasumeni ku adindo oyenera (ofesi yaboma yoona zogawa katundu wamasiye, ku khothi, kwa bwana mkubwa wa boma lanu, kwa mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, ku bungwe loona za ufulu wa anthu, kwa mkulu womva madandaulo a anthu, ku mabungwe omwe siaboma, ndi ena). |
| Wachibale | (a) Lemekezani wilo;<br>(b) Ngati kholo lamwalira lisanakonze wilo, lemekezani malamulo amene amagwiritsidwa ntchito munthu akamwalira asanalembe wilo; komanso<br>(c) Pamene mukugawira chuma mwana amene mumangomusunga koma sanali wanu, tambasulani momveka bwino chuma chomwe mukumugawira. | (a) Kasumeni kwa adindo oyenera komanso lemekezani chigamulo chawo (ofesi yaboma yogawa chuma chamasiye, kwa bwana mkubwa wa boma lanu, kwa amfumu, ku khothi, ndi ena); komanso<br>(b) Funsani uphungu kuofesi yoyenera (mabungwe omwe siaboma, anthu akudera, bungwe loona za ufulu wa anthu, ofesi yomva madandaulo a anthu ndi ena). |
| Mfumu | (a) Kulimbikitsa ndi kuzindikilitsa anthu;<br>(b) Kulemekeza malamulo okhudza chuma chamasiye; komanso<br>(c) Kuluzanitsa miyambo, zikhalidwe ndi zikhulupiriro | (a) Kuyang'anira kagawidwe ka katundu wamasiye; komansoKutumiza anthu ku ofesi yoyenera (kwa mkulu woyang'anira kagawidwe ka katundu wa masiye, kwa bwana mkubwa wa boma lanu, ku polisi, ku khothi, ku mabungwe omwe siaboma, ku bungwe loona za ufulu wa anthu, ofesi ya |

| | | |
|---|---|---|
| | ndi malamulo okhudza chuma chamasiye. | mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena). |
| Munthu wokhala m'dera | (a) Lemekezani wilo;<br>(b) Lemekezani malamulo okhudza chuma chamasiye;<br>(c) Samalani ndi kukhala tcheru ndi mchitidwe wolanda katundu; komanso<br>(d) Kasumeni mchitidwe wolanda katundu. | (a) Kasumeni kwa adindo oyenera komanso lemekezani chigamulo chawo (ofesi yaboma yogawa chuma chamasiye, kwa bwana mkubwa wa boma lanu, amfumu, ku khothi, ndi ena) komanso<br>(b) Funsani uphungu kwa adindo oyenera (mabungwe omwe siaboma, anthu akudera, bungwe loona za ufulu wa anthu, ofesi yomva madandaulo a anthu ndi ena). |

***(f) Kuzembetsa Ana***

Kuzembetsa ana ndi mchitidwe wotenga, kugulitsa, kupereka, kusunga kapena kulandira ana ndi cholinga chowagwiritsa ntchito kuti upeze phindu (kuwagwiritsa ntchito mokakamiza, kugonedwa ndi zina). Kuzembetsa ana ndi mlandu womwe chilango chake chachikulu chomwe chili kukakhala ku ndende moyo wako wonse. Munthu yemwe wapalamula mlandu umenewu sangawilingule ponena kuti mwana yemwe anamuzembetsayo anavomereza kapena amadziwa zomwe zimachitika ndi cholinga choti mlanduwu umukomere.

*Zoyenera kuchita pankhani yokhudza kuzembetsa ana:*

| Mdindo | Kupewa ndi Kuteteza | Kuchitapo Kanthu |
|---|---|---|
| Kholo | (a) Kulangiza ndi kuzindikilitsa ana za mchitidwe wozembetsa ana ndi kuwauza njira zodzitetezera;<br>(b) Kukhazikitsa kukhulupirirana ndi kudalirana pakati pa kholo ndi mwana kudzera mu zochitika zoonetsa chikondi ndi chisamaliro cha kholo;<br>(c) Kudziwa ufulu wa ana;<br>(d) Kulemekeza umunthu ndi kufunikira kwa ana;<br>(e) Kuchita kalondolondo wa kakulidwe ndi zochita za mwana;<br>(f) Kumupatsa mwana zinthu zofunikira pa moyo wake pofuna kupewa kuti anganyengeleredwe;<br>(g) Kukhazikitsa kulumikizana kwapadera ndi kwa chinsinsi pakati pa kholo ndi mwana;<br>(h) Kuperekeza mwana kapena kutuma munthu wodalirika kuti aperekeze mwana popita ndi pochokera kusukulu kapena kumulimbikitsa mwana kuti adziyenda pagulu la anzake popita ndi pochokera kusukulu; komanso<br>(i) Kulimbikitsa kusintha kwa zikhalidwe, | (a) Kutsatira nkhani yomwe yachitika imene mwana wokhudzidwa kapena munthu wina wafotokoza;<br>(b) Kusuma za mchitidwe wa nkhanza zozembetsa mwana kwa adindo oyenera (amfumu, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, apolisi, bungwe loona za ufulu wa anthu, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena); komanso<br>(c) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana wokhudzidwa. |

| | | |
|---|---|---|
| | miyambo, zikhulupiriro zoyipa ndi maganizidwe;<br>(j) Kuonetsetsa kuti mwana akusamalidwa ndi munthu woyenerera kholo likachoka pakhomo. | |
| Wachibale | (a) Kulangiza ndi kuwazindikilitsa ana za mchitidwe wozembetsa ana ndi kuwauza njira zodzitetezera;<br>(b) Kudziwa ufulu wa ana;<br>(c) Kukhazikitsa kukhulupilirana ndi kudalirana pakati pa kholo ndi mwana kudzera mu zochitika zoonetsa chikondi ndi chisamaliro cha kholo;<br>(d) Kulemekeza ndi kuteteza umunthu, moyo wabwino ndi kufunikira kwa mwana;<br>(e) Kuchita kalondolondo wa kakulidwe ndi zochita za mwana;<br>(f) Kumupatsa mwana zinthu zofunikira pa moyo wake pofuna kupewa kuti anganyengeleredwe;<br>(g) Kuperekeza mwana kapena kutuma munthu wodalirika kuti aperekeze mwana popita ndi pochokera kusukulu kapena kumulimbikitsa mwana kuti adziyenda pagulu la anzake popita ndi pochokera kusukulu;<br>(h) Kuonetsetsa kuti mwana akusamalidwa ndi munthu woyenerera iwo akachokapo komanso<br>(i) Kulimbikitsa kusintha kwa zikhalidwe, miyambo, zikhulupiriro zoyipa ndi maganizidwe; | (a) Kusuma nkhani ya mchitidwe wozembetsa ana womwe wachitika kwa adindo oyenera (apolisi, amfumu, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, ku khothi, nthambi yoona za anthu olowa ndi kutuluka m'dziko muno, bungwe loona za ufulu wa anthu, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena;<br>(b) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana yemwe wakhudzidwa;<br>(c) Kutumiza ndi kuperekeza mwana yemwe wakhudzidwa kwa anthu oyenera omwe angamuthandize (mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, apolisi, mlangizi, ndi ena); komanso<br>(d) Kulondola ndi kuwonetsetsa momwe zikuyendera nkhani za ana omwe anatumizidwa kuti akathandizidwe ndi anthu oyenera. |
| Mfumu | (a) Kukhala patsogolo polimbikitsa ndi kutsogolera kusintha kwa chikhalidwe, miyambo ndi zina;<br>(b) Kukonza ndi kukhazikitsa ndondomeko zothandiza kuonetsetsa chitetezo cha ana pamene akupita ndi kuchokera kusukulu, mwachitsanzo kutuma munthu wodalirika kuti aperekeze ana popita ndi pochokera kusukulu kapena kuwalimbikitsa ana kuti aziyenda m'magulu popita ndi pochokera kusukulu; komanso<br>(c)Kusuma zomwe zachitika kwa adindo oyenera (apolisi, amfumu wogwira ntchito | Kulondolera anthu kwa adindo oyenera (apolisi, atsogoleri a pa sukulu, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, bungwe loona za ufulu wa anthu, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena). |

| | | |
|---|---|---|
| | zosamalira anthu, bwalo la milandu, nthambi yoona za anthu olowa ndi kutuluka m'dziko muno, bungwe loona za ufulu wa anthu, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena) | |
| Munthu wokhala m'dera | (a) Kutsata malamulo othana ndi mchitidwe wozembetsa ana;<br>(b) Kudziwitsa ena nkhani zokhudza kuopsya kwa mchitidwe wozembetsa ana;<br>(c) Kuvomereza ndi kulimbikitsa zoti chikhalidwe choyipa chisinthe;<br>(d) Kuzindikira ndi kukhala tcheru ndi mchitidwe wozembetsa ana; ndi<br>(e) Kutenga nawo mbali pakulimbikitsa ndi kutengulira udindo woyang'anira mwana limodzi ndi ena kapena pawekha; komanso<br>(f) Kukonza ndi kugwiritsa ntchito njira zomwe cholinga chake ndi kuonetsetsa kuti ana ndi otetezedwa popita komanso pochokera kusukulu, mwachitsanzo kusankha munthu wodalirika woti aziperekeza ana popita ndi pochokera kusukulu kapena kuwalimbikitsa ana kuti popita ndi pochokera kusukulu aziyenda m'magulu. | (a) Kusuma mchitidwe wozembetsa ana kwa adindo oyenera (kwa a mfumu, apolisi, mkulu womva madandaulo a anthu, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, ku mabungwe omwe siaboma, ku bungwe loona za ufulu wa anthu ndi adindo ena); komanso<br>(b) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana wokhudzidwa. |
| Mphunzitsi ndi utsogoleri wa pa sukulu | (a) Kukonza ndi kukhazikitsa ndondomeko zothandiza kuonetsetsa chitetezo cha ana pamene akupita ndi kuchokera kusukulu, mwachitsanzo kutuma munthu kuti aperekeze ana popita ndi pochokera kusukulu kapena kuwalimbikitsa ana kuti aziyenda m'magulu popita ndi pochokera kusukulu;<br>(b) Kulimbikitsa malamulo othana ndi mchitidwe wozembetsa ana;<br>(c) Kulangiza ndi kuzindikiritsa ophunzira za mchitidwe ozembetsa ana njira zomwe angagwiritse ntchito zodziteteza ku mchitidwe ozembetsa ana;<br>(k) Kulimbikitsa makolo kukhazikitsa kulumikizana kwapadera ndi kwa chinsinsi pakati pa kholo ndi mwana;<br>(l) Kudziwa ufulu wa ana;<br>(m) Kulemekeza ndi kuteteza ulemu, moyo wabwino ndi kufunikira kwa mwana;<br>(n) Kuchita kalondolondo wa kakulidwe ndi zochita za mwana;<br>(o) Kulimbikitsa ndi kutsogolera zothetsa mchitidwe wozembetsa ana;<br>(p) Kuyamba kuchitapo kanthu pofuna | (a) Kunena nkhani zozembetsa ana kwa adindo oyenera (unduna wa zamaphunziro, apolisi, nthambi yoona za anthu olowa ndi kutuluka m'dziko muno, bungwe loona za ufulu wa anthu, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena);<br>(b) Kulimbikitsa kuti mphunzitsi kapena mdindo wina aliyense woganiziridwa kuti wapalamula mlandu alandire chilango;<br>(c) Kuthandiza ndi kutumiza mwana yemwe wakhudzidwa kwa anthu oyenerera (bungwe loona za ufulu wa anthu, mphunzitsi, mnzake, mlangizi,ndi ena otero); ndi |

| | | |
|---|---|---|
| | kusintha zinthu pokambirana ndi mafumu, apolisi, makolo ndi anthu a m'deralo;<br>(q) Kuvomereza, kukonza ndi kukwanilitsa ndondomeko zomwe cholinga chake ndi kuthana ndi mchitidwe wozembetsa ana; ndi<br>(r) Kukhazikitsa ndondomeko yokasumira nkhani zochitika ndi kugawana ntchito. | (d) Kulondola ndi kuonetsetsa momwe na omwe anatumizidwa kuti akathandizidwe ndi anthu oyenera zikuyendera. |

.

***(g) Kusunga Mwana Momukakamiza, Kusunga Atsikana Mowakakamiza komanso Kuba Ana***

Kusunga mwana momukakamiza ndi mchitidwe wotenga kapena kubisa mwana popanda chilolezo cha kholo kapena munthu ovomerezeka kusunga ndi kuyang'anira mwanayo. Kusunga atsikana mowakakamiza ndi mchitidwe wotenga kapena kubisa atsikana osakwanazaka 16 popanda chilolezo cha kholo kapena munthu ovomerezeka kusunga ndi kuyang'anira mtsikanayo. Kuba mwana ndi mchitidwe otenga mwana kuchokera kwa kholo kapena munthu womuyang'anira ndi cholinga choti kholo kapena munthu womuyang'anirayo asakhale mwini wa mwanayo.

*Milandu ndi zilango zomwe zimaperekedwa mokhudzana ndi mchitidwe wosunga mwana momukakamiza, kusunga atsikana mowakakamiza, ndi kuba mwana:*

| Mlandu | Chilango |
|---|---|
| Kusunga mwana momukakamiza | Kukhala ku ndende kwa zaka 10 |
| Kusunga atsikana yemwe sanakwanitse zaka 16 mowakakamiza | Kukhala ku ndende kwa zaka 7 |
| Kuba mwana | Kukhala ku ndende kwa zaka 7 |
| Kusunga munthu ndi cholinga kapena kumuyika mu nyumba ya malonda a chisembwere | Kukhala ku ndende kwa zaka zisanu |

*Zoyenera kuchita pa mchitidwe wosunga mwana momukakamiza, kusunga atsikana mowakakamiza, ndi kuba mwana*

| Mdindo | Kupewa ndi Kuteteza | Kuchitapo Kanthu |
|---|---|---|
| Kholo | (a) Kulangiza ndi kuzindikiritsa ana za mchitidwe wosunga mwana momukakamiza, kusunga atsikana mowakakamiza, ndi kuba mwana komanso kuwauza njira zodzitetezera;<br>(b) Kukhazikitsa kukhulupirirana ndi kudalirana pakati pa kholo ndi mwana kudzera mu zochitika zoonetsa chikondi ndi chisamaliro cha kholo;<br>(c) Kudziwa ufulu wa ana;<br>(d) Kulemekeza ulemu ndi kufunikira kwa ana;<br>(e) Kuchita kalondolondo wa kakulidwe ndi zochita za mwana;<br>(f) Kumupatsa mwana zinthu zofunikira pa | (a) Kutsatira nkhani yomwe yachitika imene mwana wokhudzidwa kapena munthu wina wafotokoza;<br>(b) Kusuma za mchitidwe wa nkhanza zosunga mwana momukakamiza, kusunga atsikana mowakakamiza, ndi kuba mwana kwa adindo oyenera (amfumu, mkulu woona za chisamaliro cha anthu |

| | | |
|---|---|---|
| | moyo wake pofuna kupewa kuti anganyengeleredwe;<br>(g) Kukhazikitsa kulumikizana kwapadera ndi kwa chinsinsi pakati pa kholo ndi mwana;<br>(h) Kuperekeza mwana kapena kutuma munthu wodalirika kuti aperekeze mwana popita ndi pochokera kusukulu kapena kumulimbikitsa mwana kuti adziyenda pagulu la anzake popita ndi pochokera kusukulu; komanso<br>(i) Kulimbikitsa kusintha kwa zikhalidwe, miyambo, zikhulupiriro zoyipa ndi maganizidwe;<br>(j) Kuonetsetsa kuti mwana akusamalidwa ndi munthu woyenerera kholo likachoka pakhomo. | pa boma, ku polisi, bungwe loona za ufulu wa anthu, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena); komanso<br>(d) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana wokhudzidwa. |
| Wachibale | (a) Kulangiza ndi kuzindikiritsa ana za mchitidwe wosunga mwana momukakamiza, kusunga atsikana mowakakamiza, ndi kuba mwana komanso kuwauza njira zodzitetezera<br>(b) Kudziwa ufulu wa ana;<br>(c) Kukhazikitsa kukhulupilirana ndi kudalirana pakati pa kholo ndi mwana kudzera mu zochitika zoonetsa chikondi ndi chisamaliro cha kholo;<br>(d) Kulemekeza ndi kuteteza umnthu ndi kufunikira kwa mwana;<br>(e) Kuchita kalondolondo wa kakulidwe ndi zochita za mwana;<br>(f) Kumupatsa mwana zinthu zofunikira pa moyo wake pofuna kupewa kuti anganyengerereredwe;<br>(g) Kuperekeza mwana kapena kutuma munthu wina kuti aperekeze mwana popita ndi pochokera kusukulu kapena kumulimbikitsa mwana kuti adziyenda pagulu la anzake popita ndi pochokera kusukulu;<br>(h) Kuonetsetsa kuti mwanayo akusamalidwa ndi munthu woyenerera iwo akachokapo komanso<br>(i) Kulimbikitsa kusintha kwa zikhalidwe, miyambo, zikhulupiriro zoyipa ndi maganizidwe; | (a) Kusuma nkhani ya mchitidwe wosunga mwana momukakamiza, kusunga atsikana mowakakamiza, ndi kuba mwana kwa adindo oyenera (apolisi, amfumu, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, bwalo la milandu, bungwe loona za ufulu wa anthu, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena;<br>(b) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana yemwe wakhudzidwa;<br>(c) Kutumiza ndi kuperekeza mwana yemwe wakhudzidwa kwa anthu oyenera omwe angamuthandize (mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, apolisi, mlangizi, ndi ena); komanso<br>(d) Kulondola ndi kuonetsetsa momwe nkhani za ana omwe anatumizidwa kuti akathandizidwe ndi anthu oyenera zikuyendera |

| | | |
|---|---|---|
| Mfumu | (a) Kukhala patsogolo polimbikitsa ndi kutsogolera kusintha kwa zikhalidwe miyambo yoyipa ndi zina;<br>(b) Kukonza ndi kukhazikitsa ndondomeko zothandiza kuonetsetsa chitetezo cha ana pamene akupita ndi kuchokera kusukulu, mwachitsanzo kutuma munthu kuti aperekeze ana popita ndi pochokera kusukulu kapena kuwalimbikitsa ana kuti aziyenda m'magulu popita ndi pochokera kusukulu; komanso<br>(c) Kusuma zomwe zachitika kwa adindo oyenera (apolisi, amfumu, mkulu woona za chismaliro cha anthu pa boma, ku kohthi, bungwe loona za ufulu wa anthu, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena | Kulondolera anthu kwa adindo oyenera (apolisi, atsogoleri a pasukulu, ofesi ya mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, ofesi yoona za ufulu wa anthu, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena). |
| Munthu wokhala m'dera | (a) Kutsata malamulo othana ndi mchitidwe wosunga mwana momukakamiza, kusunga atsikana mowakakamiza, ndi kuba mwana ana;<br>(b) Kudziwitsa ena za kuopsa kwa mchitidwe wosunga mwana momukakamiza, kusunga atsikana mowakakamiza, ndi kuba mwana;<br>(c) Kuvomereza ndi kulimbikitsa kuti chikhalidwe chisinthe ndi kusintha kwina;<br>(d) Kuzindikira ndi kukhala tcheru ndi mchitidwe wosunga mwana momukakamiza, kusunga atsikana mowakakamiza, ndi kuba mwana; ndi<br>(e) Kutenga mbali pakulimbikitsa ndi kutengulira udindo woyang'anira mwana limodzi ndi ena kapena pawekha; komanso<br>(f) Kukonza ndi kugwiritsa ntchito njira zomwe cholinga chake ndi kuonetsetsa kuti ana ndi otetezedwa popita komanso pochokera kusukulu, mwachitsanzo kusankha munthu wodalirika kuti aziperekeza ana popita ndi pochokera kusukulu kapena kuwalimbikitsa ana kuti popita ndi pochokera kusukulu aziyenda m'magulu. | (a) Kusuma mchitidwe wosunga mwana momukakamiza, kusunga atsikana mowakakamiza, ndi kuba mwana kwa adindo oyenera (kwa a mfumu, kupolisi, mkulu owona za chisamaliro cha anthu pa boma, mabungwe omwe siaboma, bungwe loona za ufulu wa anthu, mkulu womva madandaulo a anthu ndi ena); komanso<br>(b) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana wokhudzidwa. |
| Mphunzitsi ndi utsogoleri wa pa sukulu | (a) Kukonza ndi kukhazikitsa ndondomeko zothandiza kuwonetsetsa chitetezo cha ana pamene akupita ndi kuchokera kusukulu, mwachitsanzo kutuma munthu wadalirika kuti aperekeze ana popita ndi pochokera kusukulu kapena | (a) Kunena zosunga mwana momukakamiza, kusunga atsikana mowakakamiza, ndi kuba mwana kwa adindo oyenera (unduna wa za maphunziro, |

| | | |
|---|---|---|
| | kuwalimbikitsa ana kuti aziyenda m'magulu popita ndi pochokera kusukulu;<br>(b) Kulimbikitsa malamulo othana ndi mchitidwe wosunga mwana momukakamiza, kusunga atsikana mowakakamiza, ndi kuba mwana;<br>(c) Kulangiza ndi kuwazindikiritsa ophunzira za mchitidwe wosunga mwana momukakamiza, kusunga atsikana mowakakamiza, ndi kuba mwana ndi kuwauza njira zodzitetezera;<br>(d) Kulimbikitsa makolo kukhazikitsa kulumikizana kwapadera ndi kwa chinsinsi pakati pa kholo ndi mwana;<br>(e) Kudziwa ufulu wa ana;<br>(f) Kulemekeza ndi kuteteza umunthu ndi kufunikira kwa mwana;<br>(g) Kuchita kalondolondo wa kakulidwe ndi zochita za mwana;<br>(h) Kulimbikitsa ndi kutsogolera zothetsa mchitidwe wosunga ana muwakakamiza, kusunga atsikana mowakakamiza ndi kuba ana;<br>(i) Kuyamba kuchitapo kanthu pofuna kusintha zinthu pokambirana ndi mafumu, apolisi makolo ndi anthu a m'deralo;<br>(j) Kuvomereza, kukonza ndi kukwanilitsa ndondomeko zomwe cholinga chake ndi kuthana ndi mchitidwe wosunga ana muwakakamiza, kusunga atsikana mowakakamiza ndi kuba ana; ndi<br>(k) Kukhazikitsa ndondomeko yokasumira wosunga ana muwakakamiza, kusunga atsikana mowakakamiza ndi kuba ana ndi kugawana ntchito. | apolisi, bungwe loona za ufulu wa anthu, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena);<br>(b) Kulimbikitsa zoti mphunzitsi kapena mdindo wina aliyense amene wapalamula mlandu alandire chilango;<br>(c) Kuthandiza ndi kutumiza mwana yemwe wakhudzidwa kwa adindo oyenera (bungwe loona za ufulu wa anthu, mphunzitsi, mnzake, alangizi,ndi ena otero); ndi<br>(d) Kulondola ndi kuwonetsetsa momwe nkhani za ana omwe anatumizidwa kuti akathandizidwe ndi anthu oyenera zikuyendera. |

### (h) Tsankho Chifukwa cha Kachirombo ka HIV, Kubadwa Wamwamuna kapena Wamkazi komanso Ulumali (Kuphatikizapo Kukhala Munthu Wachilubino)

Tsankho ndi mchitidwe uliwonse wosala kapena kupatula potengera momwe munthu alili kapena zomwe mukumuganizira. Zina mwa zinthu zomwe zimabweretsa tsankho ndi: Kupezeka ndi kachirombo ka HIV, chibadwidwe, maonekedwe, ndi ulumali. Tsankho limachitika ndi cholinga chofuna kusokoneza ufulu umene munthu ali nawo.

*Milandu ndi zilango zomwe zimaperekedwa mokhudzana ndi tsankho:*

| Mlandu | Chilango |
|---|---|
| Kusala mwana chifukwa chakuti ali ndi kachirombo koyambitsa matenda a Edzi | Ngati walakwira malamulo ndi munthu - kulipira chindapusa cha K 5, 000, |

| | |
|---|---|
| | 000 komanso kukhala ku ndende zaka zisanu |
| | Ngati yalakwira malamulo ndi kampani kapena bungwe - kulipira chindapusa cha K10, 000, 000 |
| Kusala mwana chifukwa chakuti ndi mkazi kapena mamuna | Chindapusa cha K 1, 000, 000 komanso kukhala ku ndende zaka zisanu |

*Kuonjezera apo, potengera kuti anthu omwe ali ndi ulumali wachialubino akukumana ndi nkhanza zosiyanasiyana, boma linakhazikitsa milandu ndi zilango zomwe zikuteteza anthu a chialubino ku nkhanza motere:*

| Mlandu | Chilango |
|---|---|
| Kuvulaza munthu wachialubino | Kukhala kundende moyo wake wonse |
| Kuchotsa kapena kusunga ziwalo za munthu | Kukhala kundende moyo wake wonse |
| Kugulitsa thupi la munthu wakufa kapena ziwalo | Kukhala kundende moyo wake wonse |
| Kulowa kumanda kapena ku malo osungira mitembo ndi cholinga chokafukula kapena kuchotsa ziwalo | Kukhala kundende kwa zaka 21 |
| Kufukula thupi posatsata malamulo | Kukhala kundende moyo wake wonse |

*Zoyenera kuchita pankhani yokhudza mchitidwe wa tsankho:*

| Mdindo | Kupewa ndi kuteteza | Kuchitapo Kanthu |
|---|---|---|
| Kholo | (a) Kulangiza ndi kuzindikilitsa ana za mchitidwe wa tsankho;<br>(b) Kukhazikitsa kukhulupirirana ndi kudalirana pakati pa kholo ndi mwana kudzera mu zochitika zoonetsa chikondi ndi chisamaliro cha kholo;<br>(c)Kudziwa ufulu wa ana;<br>(d) Kulemekeza ulemu ndi kufunikira kwa ana;<br>(e) Kuchita kalondolondo wa mmene akukulira mwana ndi zochita za mwana;<br>(f) Kuperekeza mwana kapena kutuma munthu wodalirika kuti aperekeze mwana popita ndi pochokera kusukulu kapena kumulimbikitsa mwana kuti adziyenda pagulu la anzake popita ndi pochokera kusukulu;<br>(g) Kuonetsetsa kuti mwana akusamalidwa ndi munthu woyenerera makolo akachokapo; komanso<br>(h) Kulimbikitsa kusintha kwa zikhalidwe, | (a) Kutsatira nkhani yomwe yachitika imene mwana wokhudzidwa kapena munthu wina wafotokoza;<br>(b) Kukasuma za mchitidwe wa nkhanza za tsankho kwa adindo oyenera (amfumu, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, kupolisi, bungwe loona za ufulu wa anthu, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena); komanso<br>(c) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana wokhudzidwa<br>(d) Kuthandiza ndi kutumiza mwana yemwe wakhudzidwa kwa adindo oyenera (bungwe loona za ufulu wa anthu, mphunzitsi, mnzake, |

| | | |
|---|---|---|
| | miyambo, zikhulupiriro zoyipa ndi maganizidwe. | alangizi, ndi ena) |
| Wachibale | (a) Kulangiza ndi kuzindikilitsa ana za mchitidwe wa tsankho ndi kuwauza njira zodzitetezera;<br>(b) Kudziwa ufulu wa ana;<br>(c) Kukhazikitsa kukhulupilirana ndi kudalirana pakati pa kholo ndi mwana kudzera mu zochitika zoonetsa chikondi ndi chisamaliro cha kholo;<br>(d) Kulemekeza ndi kuteteza ulemu, moyo wabwino ndi kufunikira kwa mwana;<br>(e) Kuchita kalondolondo wa kakulidwe ndi zochita za mwana;<br>(f) Kuperekeza mwana kapena kutuma munthu wodalirika kuti aperekeze mwana popita ndi pochokera kusukulu kapena kumulimbikitsa mwana kuti adziyenda pagulu la anzake popita ndi pochokera kusukulu;<br>(g) Kuonetsetsa kuti mwanayo akusamalidwa ndi munthu woyenerera iwo akachokapo komanso<br>(h) Kulimbikitsa kusintha kwa zikhalidwe, miyambo, zikhulupiriro zoyipa ndi maganizidwe. | (a) Kusuma nkhani ya mchitidwe wa tsankho kwa adindo oyenera (apolisi, amfumu, wogwira ntchito zosamalira anthu, ku khothi, ofesi yoona za ufulu wa anthu, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena);<br>(b) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana yemwe wakhudzidwa;<br>(c) Kutumiza ndi kuperekeza mwana yemwe wakhudzidwa kwa anthu oyenera omwe angamuthandize (mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, apolisi, mlangizi, ndi ena); komanso<br>(d) Kulondola ndi kuonetsetsa momwe zikuyendera nkhani za ana omwe anatumizidwa kuti akathandizidwe ndi anthu oyenera. |
| Mfumu | (a) Kukhala patsogolo polimbikitsa ndi kutsogolera kusintha kwa chikhalidwe, miyambo ndi zina;<br>(b) Kukonza ndi kukhazikitsa ndondomeko zothandiza kuonetsetsa chitetezo cha ana pamene akupita ndi kuchokera kusukulu, mwachitsanzo kutuma munthu wodalirika kuti aperekeze ana popita ndi pochokera kusukulu kapena kuwalimbikitsa ana kuti aziyenda m'magulu popita ndi pochokera kusukulu;<br>(c) Kulimbikitsa malamulo olimbana ndi mchitidwe wa tsankho komanso<br>(d) Kusuma nkhanza za tsankho kwa adindo oyenera (utsogoleri wa pasukulu, mkulu waboma woona za chisamaliro cha anthu, ofesi yoona za ufulu wa anthu, mkulu wa ofesi yomva za madandaulo a anthu ndi ena) | Kulondolera anthu kwa adindo oyenera (apolisi, atsogoleri pa sukulu, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, bungwe loona za ufulu wa anthu, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena) |
| Munthu wokhala m'dera | (a) Kudziwa malamulo okhudza tsankho<br>(b) Kugawana ndi anthu ena mauthenga okhudza kuopsya kwa tsankho;<br>(c) Kuvomereza ndi kulimbikitsa kusintha | (a) Kusuma mchitidwe wa tsankho kwa adindo oyenera (kwa a mfumu, apolisi, mkulu owona za chisamaliro cha |

| | | |
|---|---|---|
| | kwa maganizidwe;<br>(d) Kuvomereza, kuyikiza mwa ena ndi kulimbikitsa udindo wosamala ana, ngati gulu mothandizana kapena aliyense payekhapayekha;<br>(e) Kuzindikira ndi kukhala tcheru ndi zinthu zina zomwe zingachitike zokhudza mchitidwe wa tsankho; komanso<br>(f) Kukonza ndi kukwanilitsa ndondomeko zoonetsetsa kuti mwana ndiwotetezedwa kunyumba, kusukulu komanso pamene akuyenda kupita ndi kuchokera kusukulu, mwachitsanzo kutuma munthu wodalirika kuti aperekeze ana popita ndi kuchokera kusukulu kapena kuwalimbikitsa ana kuti adziyenda m'magulu popita ndi pochokera kusukulu. | anthu pa boma, mkulu womva madandaulo a anthu, ku mabungwe omwe siaboma, bungwe loona za ufulu wa anthu, ndi ena); komanso<br>(b) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana wokhudzidwa. |
| Mphunzitsi ndi utsogoleri wa pa sukulu | (a) Kukonza ndi kukhazikitsa ndondomeko zothandiza kuonetsetsa chitetezo cha ana pamene akupita ndi kuchokera kusukulu, mwachitsanzo kutuma munthu kuti aperekeze ana popita ndi pochokera kusukulu kapena kuwalimbikitsa ana kuti aziyenda m'magulu popita ndi pochokera kusukulu;<br>(b) Kulimbikitsa ndi kutsogolera ntchito yothana ndi mchitidwe wa tsankho<br>(c) Kuwatsogolera ana ndi kuwazindikiritsa za mchitidwe wa tsankho ndi momwe angazitetezere;<br>(d) Kudziwa ufulu wa ana;<br>(e) Kulemekeza umunthu ndi kufunikira kwa ana;<br>(f) Kuchita kalondolondo wa kakulidwe ndi zochita za mwana;<br>(g) Kugwira ntchito ndi mafumu, apolisi, makolo ndi anthu akudera;<br>(h) Kuvomereza, kukonza ndi kukwanilitsa ndondomeko zomwe cholinga chake ndi kuthana ndi mchitidwe wa tsankho;<br>(i) Kusuma mchitidwe wa tsankho kwa anthu ndi mabungwe oyenera (apolisi, ofesi ya mkulu waboma woona za chisamaliro cha anthu, ofesi yoona za ufulu wa anthu, ofesi yomva madandawulo a anthu ndi ena); komanso<br>(j) Kukhazikitsa ndondomeko zothandiza ana okhudzidwa kukanena komanso kugawana ntchito. | (a) Kuwonetsetsa kuti malo ophunzilira ana a sukulu ndi wotetezedwa komanso osavuta kufikira; komanso<br>(b) Kuchita kalondolondo wankhani zomwe zasumidwa zokhudza tsankho. |

### (i) *Mchitidwe Woyipa ndi Miyambo Yoyipa (*Wokhudza Kusiyanitsa Pakati pa Nchito za Munthu Wamkazi ndi Wamwamuna*, Kachirombo ka HIV ndi Kasamalidwe ka Ana)*

Mchitidwe woyipa ndi mchitidwe wokhudza chikhalidwe, miyambo kapena zipembedzo umene potengera chibadwidwe, kusiyanitsa pakati pa nchito za munthu wamkazi ndi wamwamuna, kukhala kapena kusakhala pabanja umayang'anira kapena ungathe kuyang'anira pansi ulemu wa munthu, thanzi lake ufulu wake, kapenanso kuchititsa munthu kuvulala pathupi, nkhani zogonana kapena m'maganizo. Mwambo woyipa ndi mchitidwe wokhudza miyambo womwe uli oopsya ku thanzi la mwana ndi makulidwe ake.

Lamulo limateteza ana ku mchitidwe woyipa ndi miyambo yoyipa yosiyanasiyana.

*Milandu ndi zilango zomwe zimaperekedwa zokhudzana ndi mchitidwe ndi miyambo yoyipa:*

| Mlandu | Chilango |
|---|---|
| Mchitidwe woyipa (wokhudza kusiyanitsa pakati pa ntchito za munthu wamkazi ndi wamwamuna) | Kulipira chindapusa cha ndalama zokwana K1,000,000 ndi kukhala mundende zaka zisanu |
| Mchitidwe woyipa (wokhudza kachirombo ka HIV) | Kulipira chindapusa cha ndalama zokwana K5,000,000 ndi kukhala mundende kwa zaka zisanu |
| Miyambo yoyipa (yokhudza chisamaliro cha mwana) | Kukhala mundende zaka 10 |

*Zoyenera kuchita pankhani zokhudza mchitidwe woyipa ndi miyambo ya makololo yoopsya*

| Mdindo | Kupewa ndi kuteteza | Kuchitapo Kanthu |
|---|---|---|
| Kholo | (a) Kulangiza ndi kuzindikilitsa ana za mchitidwe woyipa ndi miyambo yoyipa pa moyo wawo ndi makulidwe awo;<br>(b) Kudziwa ufulu wa ana;<br>(c) Kulemekeza umunthu ndi kufunikira kwa ana;<br>(d) Kuchita kalondolondo wa kakulidwe ndi zochita za mwana;<br>(e) Kukana kutenga nawo mbali mu mchitidwe woyipa ndi miyambo yoyipa<br>(f) Kuonetsetsa kuti mwana akusamalidwa ndi munthu oyenera makolo akachokapo;<br>(g) Kuperekeza mwana kapena kutuma munthu wodalirika kuti aperekeze mwana popita ndi pochokera kusukulu kapena | (a) Kutsatira nkhani ya mchitidwe woyipa kapena miyambo imene mwana wokhudzidwa kapena munthu wina wafotokoza;<br>(b) Kusuma za mchitidwe woyipa kapena miyambo yoyipa kwa adindo oyenera (amfumu, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, kupolisi, bungwe loona za ufulu wa anthu, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi |

| | | |
|---|---|---|
| | kumulimbikitsa mwana kuti adziyenda pagulu la anzake popita ndi pochokera kusukulu; komanso<br>(h) Kulimbikitsa kusintha kwa zikhalidwe, miyambo, zikhulupiriro zoyipa ndi maganizidwe. | ena);<br>(c) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana wokhudzidwa; komanso<br>(d) Kuthandiza ndi kutumiza mwana yemwe wakhudzidwa kwa anthu oyenerera (polisi, mfumu, bungwe loona za ufulu wa anthu, bungwe loona za kachirombo ka HIV ndi matenda a Edzi, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu ndi ena) |
| Wachibale | (a) Kulangiza ndi kuwazindikiritsa za kuopsya kwa mchitidwe woyipa ndi miyambo yoyipa pa moyo wawo ndi makulidwe awo;<br>(b) Kukhazikitsa kukhulupilirana ndi kudalirana pakati pa kholo ndi mwana kudzera mu zochitika zoonetsa chikondi ndi chisamaliro cha kholo;<br>(c) Kudziwa ufulu wa ana;<br>(d) Kulemekeza ndi kuteteza umunthu ndi kufunikira kwa mwana;<br>(e) Kuchita kalondolondo wa kakulidwe ndi zochita za mwana;<br>(f) Kukana kutenga nawo mbali mu mchitidwe woyipa kapena miyambo yoyipa;<br>(g) Kuonetsetsa kuti mwana akusamalidwa ndi munthu woyenerera makolo akachokapo;<br>(h) Kuperekeza mwana kapena kutuma munthu wodalirika kuti aperekeze mwana popita ndi pochokera kusukulu kapena kumulimbikitsa mwana kuti adziyenda pagulu la anzake popita ndi pochokera kusukulu; komanso<br>(i) Kulimbikitsa kusintha kwa zikhalidwe, miyambo, zikhulupiriro zoyipa ndi maganizidwe. | (a) Kutsatira nkhani ya mchitidwe woyipa kapena miyambo yoyipa imene mwana wokhudzidwa kapena munthu wina wafotokoza;<br>(b) Kusuma nkhani ya mchitidwe woyipa kapena miyambo yoyipa yomwe yachitika kwa adindo oyenera (apolisi, mfumu, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, bungwe loona za kachirombo ka HIV ndi matenda a Edzi, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, bungwe loona za ufulu wa anthu, ndi ena;<br>(c) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana yemwe wakhudzidwa;<br>(d) Kutumiza ndi kuperekeza mwana yemwe wakhudzidwa kwa adindo oyenera omwe angamuthandize (apolisi, mfumu, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, bungwe loona za ufulu wa anthu, bungwe lolimbana za kachirombo ka HIV ndi matenda a Edzi, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena |

| | | |
|---|---|---|
| Mfumu | (a) Kukhala patsogolo polimbikitsa ndi kutsogolera kusintha kwa chikhalidwe, miyambo ndi zina;<br>(b) Kukonza ndi kukhazikitsa ndondomeko zothandiza kuwonetsetsa chitetezo cha ana pamene akupita ndi kuchokera kusukulu, mwachitsanzo kutuma munthu kuti aperekeze ana popita ndi pochokera kusukulu kapena kuwalimbikitsa ana kuti aziyenda m'magulu popita ndi pochokera kusukulu;<br>(c) Kulimbikitsa malamulo olimbana ndi mchitidwe woyipa kapena miyambo yoyipa; komanso<br>(d) Kusuma nkhanza kwa adindo oyenera (polisi, mfumu, mkulu woyang'anira za ana, bungwe loona za ufulu wa anthu, bungwe loona za kachirombo ka HIV ndi matenda a Edzi, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena). | (a) Kuletsa mchitidwe kapena mwambo woyipa; ndi<br>(b) Kulondolera anthu kwa adindo oyenera (apolisi, mfumu yayikulu, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, bungwe loona za ufulu wa anthu, bungwe loona za kachirombo ka HIV ndi matenda a Edzi, ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, ndi ena) |
| Munthu okhala m'dera | (a) Kudziwa malamulo okhudza mchitidwe ndi miyambo yoyipa;<br>(b) Kugawana ndi anthu ena mauthenga okhudza kuopsya kwa mchitidwe woyipa ndi miyambo yoyipa;<br>(c) Kuvomereza ndi kulimbikitsa kusintha kwa maganizidwe;<br>(d) Kuvomereza, kuyikiza mwa ena ndi kulimbikitsa udindo wosamala ana, ngati gulu mothandizana kapena aliyense payekhapayekha;<br>(e) Kuzindikira ndi kukhala tcheru ndi zinthu zina zomwe zingachitike zokhudza mchitidwe woyipa ndi miyambo yoyipa; komanso<br>(f) Kukonza ndi kukwanilitsa ndondomeko zoonetsetsa kuti mwana ndiwotetezedwa kunyumba, kusukulu komanso pamene akuyenda kupita ndi kuchokera kusukulu, mwachitsanzo kutuma munthu kuti aperekeze ana popita ndi kuchokera kusukulu kapena kuwalimbikitsa ana kuti adziyenda m'magulu popita ndi pochokera kusukulu | (a) Kusuma za mchitidwe woyipa ndi miyambo yoyipa kwa adindo oyenera (kwa a polisi, amfumu, kwa mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, mabungwe omwe siaboma, bungwe loona za ufulu wa anthu, bungwe lowona za kachirombo ka HIV ndi matenda a Edzi, mkulu womva madandaulo a anthu ndi ena); komanso<br>(b) Kuthandiza ndi kulimbikitsa mwana wokhudzidwa. |
| Mphunzitsi ndi utsogoleri | (a) Kulimbikitsa ndi kudziwitsa anthu ndondomeko zoletsa mchitidwe woyipa ndi zikhalidwe zoyipa.<br>(b) Kuwazindikilitsa ana ndi kuwaphunzitsa | (a) Kusuma nkhanza iyilonse yokhudzana ndi mchitidwe komanso miyambo yoyipa kwa adindo oyenera monga |

| | | |
|---|---|---|
| wa pasukulu | kuyipa kwa mchitidwe ndi zikhalidwe zoyipa;<br>(c) Kuzizindikilitsa ufulu wa ana;<br>(d) Kulemekeza umunthu wa mwana.<br>(e) Kuchita kalondolondo wa kakulidwe ndi zochita za mwana;<br>(f) Kulimbikitsa ntchito zolimbana ndi mchitidwe ndi makhalidwe oyipa;<br>(g) Kugwira ntchito mokwanira ndi anthu ena okhudzidwa monga mafumu, achitetezo, makolo ndi anthu okhala m'mudzi;<br>(h) Kuvomereza, kukonza ndi kukhazikitsa njira zosiyanasiyana pofuna kuthetsa mchitidwe oyipa komanso zikhalidwe zoyipa**;**<br>(i) Kukhazikitsa njira zoti mwana athe kukanena akakumana ndi nkhanza;<br>(j) Kukonza njira zoonetsetsa kuti ana akutetezedwa nthawi zonse; komanso<br>(k) Kulondoloza nkhani zokhudza mchitidwe oyipa ndi zikhalidwe zoyipa. | ku unduna wa zamaphunziro, ku bungwe loona za kachirombo ka HIV ndi matenda a Edzi, ku polisi, ku mabwalo a milandu, kwa mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, ku office yomva madandaulo a anthu ndi ena ambiri;<br>(b) Kulimbikitsa zilango kwa mphunzitsi kapena mkulu oyendetsa ntchito za sukulu yemwe waphwanya ufulu wa mwana;<br>(c) Kuthandiza mwana yemwe wakhudzidwa pomupititsa ku bungwe loona za ntchito yolimbana ndi kachirombo ka HIV ndi matenda a Edzi, kwa mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, a polisi, mabwalo amilandu komanso alangizi; komanso<br>(d) Kuchita kalondolondo wa momwe mwana akukhalira ku malo komwe watumizidwa. |
| Abambo olimbikitsa ntchito zolimbana ndi mchitidwe woyipa m'mudzi (Male Champion) | (a) Kudziwitsa anthu zambiri zokhudza mchitidwe woyipa;<br>(b) Kuyang'anira ndi kulimbikitsa kasinthidwe kochita zinthu;<br>(c) Kukhazikitsa malo ophunzirira ndi kukambirana; ndi<br>(d) Kuthandiza ndi kulangiza makolo, osamalira ana, utsogoleri wa pasukulu komanso mafumu pounika nkhani zokhuzana ndi mchitidwe woipa ndi chikhalidwe choyipa. | (a) Kusuma nkhanza zokhudza mchitidwe komanso zikhalidwe zoyipa kwa adindo oyenera monga ku bungwe loona za kachirombo ka HIV ndi matenda a Edzi, mkulu woona za chisamaliro cha anthu pa boma, ku polisi, alangizi ndi ena ambiri;<br>(b) Kulondoloza nkhani zomwe zinakanenedwa kale; ndi<br>(c) Ngati pali kuthekera, kutenga mbali pofuna kuthana ndi mchitidwe woyipa komanso zikhalidwe zoyipa. |